



THE MALOMO ZONE EXAMINATIONS BOARD

2021 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

CHICHEWA

(Malikisi 100)

Subject Number: PO32

Time Allowed: 2 h 15 mins

1:00- 3:15 pm

Dzina lanu: _____

Dzina la sukulu yanu: _____

Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi awiri.

2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: Gawo A, B, C ndi D.

3. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu yanu pamwamba patsamba lino.

4. Lembani chimangilizo kapena kalata mu Gawo A ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo B, C ndi D

5. Lembani yankho la mu Gawo A pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu Gawoli

6. Yankhani mafunso a mu Gawo B ndi C m` mipata yomwe yaperekedwa pansu pa funso lililonse.

7. Yankhani mafunso a mu Gawo D pozunguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.

8. Muchitebulo chilli pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

9. Perekani kwa okuyang`anirani kulemba mayeso (imvijireta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

Funso	Chongani Zomwe mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6--10			
11--15			
16-20			
21-25			
26-30			
31-35			
36-40			
41-45			

Gawo A (Malikisi 30)

Langizo: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m`munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata . Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu (MUDZI WATHU). Mwazina tsatani izi polemba.

Ndime yayamba

- Dzina lamudzi wanu
- Dera lomwe mudzi wanu uli.
- Boma lomwe mudzi wanu uli.

Ndime yachiwiri

- Mtundu wa anthu omwe ali m`mudzi mwanu.
- Chiyankhulo chomwe chimayankhulidwa m`mudzi mwanu
- Njira zomwe anthu a m`mudzi mwanu amapezera chuma chawo.

Ndime yachitatu

- Chitukuko chomwe chimachitika m`mudzi wanu
- Ubwino wachitukuko chomwe chikuchitika m`mudzi mwanu.

KAPENA

2. Lembani kalata kwa makolo anu yopempha kuti akugulireni zina mwazipangizo zophunzirira zomwe zikuthndizeni pa maphunziro anu. Mwazina tsatani izi polemba kalata yanu.

Ndime yoyamba

- Zipangizo zomwe zikufunika.
- Komwe zipangizozo zikupezeka

Ndime yachiwiri

- Momwe mudzagwiritsire ntchito zipangizozo
- Momwe mungadasamalire zipangizozo

Ndime yachitatu

- Fotokozano momwe zipangizozo zidzakuthandizireni.
- Zotsatira zomwe zingadze ngati zipangizozo sizigulidwa.

GAWO B (Malikisi 20)**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

Mudzi wa Chimtengo mudali anyamata awiri; Zingalume ndi Thokozani. Iwowa adali a nthenga imodzi ndipo adali paubwenzi wa ponda apa nane mpondepo. Anyamatawa ankasewera limodzi masewero osiyanasiyana. Ngakhale makolo awo sadali paubwenzi wotere, padalibe mangawa ena aliwonse.

Tsiku lina mwachizolowezi, anyamatatwa adapita kukasewera. Adayamba kuonyerana dzaye. Masewero atafika pa mponda chimera, aliyense adayiwala kuti dzaye ndi mwala omwe. Mwatsoka Thokozani ataponya lidakagwera pa mwendo wa Zingalume. Posakhalitsa zingalume adapsa mtima. “Sunganipweteke chotere. Lero uwona,” adatero zingalume. “pepa ambwana ine sindidachitire dala ayi,” adatero Thokozani monvetsa chisoni. Nthawi yomweyo Zingalume adaliponya khofi ndipo Thokozani adalewa ngati mphaka. Adaponyanso chibakera koma mzakeyo adalewanso. Chifukwa cha mphanvu yachibakeracho, Zingalume adagwanacho yekha. Mwatsoka adakagwera pachipanda ndipo chidamulasa patsaya.

Posakhalitsa zingalume adayamba kulira. Pamene izi zimachitika, nkuti Bengo akudya poteropo. Iye atafika adamudzutsa koma adali atavulala koopsa. “Iwe tafotokoza chomwe chatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga.” Thokozani adafokoza momwe zidayendera. “Myamata iwe zomwe akunena mzakoyu ndi zoon?” a Bengo adamufunsa. Mmalo mofotokoza iye adachitangati atsutsula pachilonda ndipo adalira kwambiri kuti makolo ake amve.

Pakuti mwana sasowa make, posakhalitsa anachisale adatulukira. Atangowona, adayamba kukalipa. “Ndimafuna iwe mwana wako wavulaza mwana wanga. Lero undidziwa kuti ndine Nachisale.” Posakhalitsa mkangano udakula. Amayi a Thokozani atawona kuti alephera kukhalirana pansi adapita kwa mfumu kukadandawula kuti awayanjanitse. Mayi Nachisale sadatheke. “mfumu muliyapa, mwana wanga akangofa, winaso atsamira mkono.” Maanja awiri adayamba kukhala mowopana. Anyamata aja sankachezeranaso ngati kale chifukwa choopa makolo awo.

MAFUNSO

a. Kodi Thokozani ndi Zingalume amakhala kuti?

_____ (malikisi 1)

b. Ndimasewera ati omwe anyamatawa ankachita?

_____ (malikisi 1)

c. Nchifukwa chiyani Zingalume adapsa mtima?

_____ (malikisi 1)

d. N`chifukwa chiyani Zingalume adalira kwambiri pomwe a Bengo amamudzutsa?

_____ (malikisi 2)

e. “Mwana wanga akangofa, winanso atsamira mkono” kodi mawuwa adayankhula ndi ndani?

_____ (malikisi 1)

f. Kodi ndiyani yemwe adadzutsa Zingalume?

_____ (malikisi 1)

- g. Pezani mikuluwiko yomwe matanthauzo ndi awa:
- i) Chinthu chomwe chayambitsa zinthu _____ (malikisi 2)
 - ii) Kufika posangalatsa kwambiri _____ (malikisi 2)
 - iii) Kukwezereza zinthu _____ (malikisi 2)
- h. Kuchokera mnkhaniyi pezani mawu otsutsana m`matanthauzo ndi awa:
- i) Kuwakhirana _____ (malikisi 1)
 - ii) Mgwirizano _____ (malikisi 1)
- i. Nchifukwa chiyani anyamatawa adasiya kuchezerana?

_____ (malikisi 2)
- j. Perekani mutu wa nkhani yomwe mwawerengayi.

_____ (malikisi 2)

GAWO C (malikisi 10)

Yankani mafunso onse awiri

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

Ambewe : Odi! Odi! Kuno.

Namulangeni: Eee! Afike mnyumba momuno.

A Mbewe : kaya munagonanawo bwanji odwalawa?

Namulangeni : Mmm! Sanatione tulo mpang`ono pomwe achezera kubuula usiku onse.

MAFUNSO

- a. (i) Tchulani mtundu wamalonje omwe mwawerengawu?
_____ (malikisi 1)
- (ii) Kodi a Namulangeni ndi ndani m`malonjewa?
_____ (malikisi 1)
- b. Perekani njira imodzi yotsatsira malonda?
_____ (malikisi 1)
- c. Lembani Malamulo awiri omwe muyenera kutsata pasukulu

_____ (malikisi 2)

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa: (malikisi 5)

a. Kumunda

b. Khwasula

c. Thidzimula

d. Kwa

e. Ngakhale

GAWO D (malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) mmfunso otsatirawa mu mgawo lino.

Mafunso 6 mpaka 10; sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo mziganzo zotsatirazi.

6. Sanabwere kusukulu poti wadwala.

- A. Mneni
- B. Mlowamalo
- C. Mlumikizi
- D. Mvekero

7. Zuze amakonda kulemba.

- A. Mneni
- B. Mfotokozi
- C. Mlowamalo
- D. Dzina

8. Nasibeko ndi wachimasomaso.

- A. Mlumikizi
- B. Mneni
- C. Mvekero
- D. Mlowamalo

9. Zingapo zafa.

- A. Mlowamalo
- B. Dzina
- C. Mperekezi
- D. Mfotokozi

10. Kalanga ine! Anthu onse atha psiti.

- A. Mfuwu
- B. Mvekero
- C. Muonjezi
- D. Mneni

Mafunso 11 mpaka 15, sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo mziganzo zotsatirazi.

11. Ndege yafika nthawi yabwino.

- A. U – Ma
- B. Li – Ma
- C. I – Zi
- D. Mu – Wa

12. Mavuto akuchokera ku msika ndi a malume

- A. Mu – A
- B. Chi – Zi
- C. Li – Ma
- D. I – Zi

13. Lamulo liposa mphanvu

- A. U – Ma
- B. Li – Ma
- C. Ka – ti
- D. I – Zi

14. Kadzidzi watera pa denga.

- A. Mu – A
- B. Ka – ti
- C. Chi – Zi
- D. I – zi

15. Mnyamata akupita kumtsinje

- A. Ku – Ma
- B. Mu – Wa

- C. Mu – Mi
- D. Ku-pa-mu

Mafunso 16 mpaka 20, sankhani chachimuna cha zinthu zomwe zatsekedwa mzere kungsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

16. Maria wagula thadzi.
 - A. Msoti
 - B. Mikolongwe
 - C. Tambala
 - D. Chipsolopsolo
17. Iye amakonda kachazi.
 - A. Msoti
 - B. Mndira
 - C. Nkhululu
 - D. Mzambwe
18. Amayi agulitsa mkota uja.
 - A. Msululu
 - B. Toned
 - C. Nkhuzi
 - D. Mbuzi
19. Madalo ndi mtsikana.
 - A. Mnyamata
 - B. Buthu
 - C. Bambo
 - D. Mzimayi
20. Iye akuti ndimupatsa nkhunda
 - A. Njiwa
 - B. Msoti
 - C. Chiwunda
 - D. Mzambwe

Mafunso 21 mpaka 23, sankhani matanthauzo a ndagi zotsatirazi.

21. Kampeni kotepatepa kaboola denga
 - A. Leza
 - B. Singano
 - C. Moto
 - D. Utsi
22. Kankhalamba aka usasamba
 - A. Mthiko
 - B. Msomba
 - C. Chule
 - D. chipande
23. walira atadzimenya yekha.
 - A. Mwana
 - B. Tambala

- C. Ng`oma
- D. Bulu

Mafunso 24 mpaka 25, sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za mkalembedwe.

24.
 - A. Yesaya wagula mbatata, sopo ndi nsomba
 - B. Yesaya wagula mbatata, sopo ndi nsomba.
 - C. Yesaya wagula mbatata sopo ndi nsomba
 - D. yesaya wagula mbatata, sopo ndi nsomba
25.
 - A. Ha, kaledi silibwerera.
 - B. Ha kaledi silibwerera
 - C. Ha! kaledi silibwerera.
 - D. ‘Ha! kaledi silibwerera.

Mafunso 26 mpaka 30, tsirizani mikuluwiko ndi mawu oyenera mziganizo zotsatirazi

26. Mlendo ndi _____
 - A. Mame
 - B. Mfumu
 - C. Bwenzi
 - D. Mwezi
27. Akula vumbwe otantha pa _____
 - A. Udzu
 - B. Tebulo
 - C. Msungwi
 - D. Tsekera
28. Safunsa adadya _____
 - A. Zowola
 - B. Nkute
 - C. Phula
 - D. Njoka
29. Khoswe wapadenga adaulura wa _____.
 - A. Mnyumba
 - B. Padzala
 - C. Mnkhekwe
 - D. Kudzenje
30. Chimvano chamavu choning`a _____
 - A. Pamimba
 - B. Pachifuwa
 - C. Pamwendo
 - D. Pakhosi

Mafunso 31 mpaka 35, sankhani nthawi ya mneni yemwe watsekedwa mzere kungsi kwawo

31. Iwo ankadzalima kuno.

- A. Yakale
 - B. Yamtsogolo
 - C. Yangothayi
 - D. Yakale yopitirira
32. Ana awa amabwerabwera kumudzi
- A. Yamtsogolo
 - B. Yakale
 - C. Yakawirikawiri
 - D. Yatsopano yangothayi
33. Agogo adzabwera chaka chamawa.
- A. Yatsopano
 - B. Yatsopano yopitirira
 - C. Yakale
 - D. Yamtsogolo
34. Iye akudya pang`onopang`ono
- A. Yakawirikawiri
 - B. Yatsopano
 - C. Yopitirira
 - D. Yamtsogolo
35. Achisale adadzaona ana awo kumudzi
- A. Yakale
 - B. Yamtsogolo yopitirira
 - C. Yakawirikawiri
 - D. Yakale yangothayi

Mafunso 36 mpaka 40, sankhani mitundu ya alowam`malo omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo.

36. Uku ndi kwathu.
- A. Owerenga
 - B. Ofunsa
 - C. Opatula
 - D. Oloza
37. Zake zapita.
- A. Opatula
 - B. Waumwini
 - C. Odzichitira
 - D. Owerenga
38. Ine ndipita mawa
- A. Oloza
 - B. Owerenga

- C. Wadzina lakelake
 - D. Waumwini
39. Amene walembe nawo, akhoza.
- A. Owerenga
 - B. Woloza
 - C. Wamgwirizano
 - D. Wakaloza wina
40. Mwatenga ziti?
- A. Wofunsa
 - B. Woloza
 - C. Owerenga
 - D. Waumwini

Mafunso 41 mpaka 45, sankhani mawu ofanana m`matanthauzo ndi mawu omwe mwapatsidwa.

41. Bilimankhwe
- A. Buluzi
 - B. Khwakhwawe
 - C. Tonkhwetonkhwe
 - D. Bongololo
42. Chamba
- A. Mankhwala
 - B. Fodya
 - C. Therere
 - D. Mfutso
43. Nkhanga
- A. Nkhwali
 - B. Njiwa
 - C. Nkhawena
 - D. Bakha
44. Chinangwa
- A. Mbatata
 - B. Kachewere
 - C. Chikhawo
 - D. Mbwani
45. Mtudzu
- A. Mtoliro
 - B. Mwano
 - C. Nkhutukumve
 - D. Tsizinamtale

MAFUNSO ATHERA APA